# Idzani Muone



Willie T. Zingani

# Idzani Muone

Wolemba:
**Willie T. Zingani**

**Chichewa Creative Series**

Published by:

Christian Literature Association in Malawi
P O Box 503
BLANTYRE
Malawi

Cover design: Brian Hara
(c) Willie T. Zingani 1990
First published 1990

No part of this book may be reproduced in any form, by print, microfilm or any means without written permission from the publisher.



## Za M'katimu

Mawu Oyamba .......... iv
1. Nkhani za Kumudzi .......... 7
2. Imfa ya Ng'anga .......... 12
3. Kunja Kwaopsa .......... 16
4. Kunsi kwa Mulatho .......... 20
5. Malo Ogona .......... 23
6. Ganyu Yosinja .......... 29
7. Osauka Satopa .......... 33
8. Chikondi cha Kumowa .......... 38
9. Alowa M'banja .......... 42
10. Chikumbumtima .......... 46
11. Mwamuna Wachipongwe .......... 50
12. Chithunzi cha Mkamwini .......... 55

# Mawu Oyamba

Malingaliro omwe ndagwiritsira ntchito m'nkhaniyi ndidawapeza kuchokera m'kucheza kwanga ndi mnzanga wapamtima, Benedicto Wokomaatani Malunga yemwe ndi munthu wotchuka kwambiri pa luntha lolemba ndakatulo.

Nthawi zina n'kwapafupi kuwerenga nthano ndi kuitenga ngati nkhani yopeka chabe. Ndifuna kukupemphani awerengi kuti ngakhale zomwe ndalemba m'bukhu la 'Idzani Muone' ndi zochokera m'mutu, chingakhale chinthu chothandiza mutaitenga nkhaniyi mozama ndi kugwirizana nane kuti zoterezi zikhozadi kuchitika kwa munthu yemwe moyo wake ngothamangathamanga.

Mkazi wanga Annie ndi anzanga awa:- Andrea Donner (wa ku Holland, koma adagwirapo ntchito kuno ku Malawi) ndi Eric Mabedi, mnyamata wotchuka pamasewera azisudzo, adandithandiza kwambiri patsutsana nane mu zina ndi zina. Kuchokera m'kutsutsana kumeneku ndidakonza mwina momwe poyamba simudali kumveka bwino.

Sinditha kutchula maina a awerengi a mabuku anga omwe kawirikawiri amandiyimitsa pamsewu, kapena kubwera kunyumba kwanga ndi malangizo a momwe ndingapitirizire patsogolo ntchito yolembayi. Abale ndi alongo dziwani kuti ndinu a mtengo wapatali. Popanda



inu ndiye kuti kulemba kwanga kulibe phindu. Zikomo kwambiri.

**Willie T. Zingani**

MUTU 1

## Nkhani za Kumudzi

Kudera la nyanja yaikulu dzina lake Maji ndi malo otentha kwambiri. Sichachilendo kuona akazi akumayenda atangovala zilundu, kumtunda kuli mbee. Ana nawonso savutika nkuvala. Amangokhala balala asadavale chilichonse. Okulirapo amakonda kumakasewera kunyanja.

Alendo ochokera kumapiri kozizira amathedwa nzeru akafika kudera la nyanjayi chifukwa chakuti kwawo palibe ndi mkazi mmodzi yemwe angayerekeze kumayenda mabere ali pamtunda.

Mudzi wotchuka wa Mondwe uli m'mbali mwa nyanjayi. Kalelo mudziwu udali wodziwika pa zinthu zambiri. Ngakhale lero lino ukacheza ndi amvula zakale amasimbapo nkhani zingapo zodabwitsa. Zambiri zoopsa zosafunika kuzimva usiku kuopa kuvutika ndi maloto.

Akutitu kalelo ku Mondwe munthu wina atafa adadzauka mkango. Musadzayerekeze kuwatsutsa akuluakulu za nkhaniyi. Adzakuuzani kuti mudziwa chiyani inu ana obadwa dzulodzulo? Ana akhanda inu nkuyamwa komwe simudasiye. Mudziwa chiyani inu ana oti pamchombo sipadaume? Makanda achabechabe ndi paliwombo pomwe sipadakhwime. Tsonotu sibwino kuwatsutsa akayamba kukuuzani zakale. Mukazindikira kuti akuluwo nkhani zawozo akuoneka ngati akuikamo mchere wambiri inu mungokhala phee nkungozisunga mumtima.

Mwati munthu atafa adadzauka mkango? Zidatani? Kodi adali wokhwima? Nkhani yoopsa iyi. Thupi lonse lingoti zii. Mwachita bwino kuiyambitsa masana, sinkhani ya usiku imeneyi.

Inde wananu ku Mondwe kudali n'ganga yotchuka dzina lake Chipolopolo. Imati ikakwiya nkumuuza munthu kuti dzuwa silimulowera basi ulendo umakhaladi omwewo. Aphwanga Chipolopolo sadali wamasewera. Iye ndiwo amadya mfutso wa nyama ya anthu. Timakanda amangobwira ngati ngumbi.

Chaka china chake Chipolopolo akuti adachita zozizwitsa. Anthu awiri m'mudzimo adakangana chifukwa cha malire a munda. Mmodzi wa iwo adapita kwa Chipolopolo. Lisadalowe dzuwa munthu winayo anali ali kulichete. Nkhani yonse idavutira pamalipiro a ntchitoyi.

"Mmene udzikafika kunyumba mnzakoyo akhala atasiya kupuma," adatero Chipolopolo kwa munthu wodzasumayo.

"Mwagwira ntchito," adayamika wodzasumayo. "Munda umene uja adatisiyira agogo athu. Iye uja ngobwera. Mwandithandiza kwambiri."

"Tsono tikambe za malipiro ake," adatero Chipolopolo.

"Eeee.. Mfumu yanga. Nenani ndibweretse nkhuku zingati?"

"Maliro a mnzakoyo akhala oika mawa," adalongosola Chipolopolo. "Zikatero iwe usiku omwewo kapite kumanda ndifuna ukandibweretsere mtima wake ndili nawo ntchito."

"Mwati chiyani?" Adafunsa wodzasumayo mwamantha.

"Wamva zomwe ndanena, usandifunse dala. Tiye pita mwamsanga."

"Ayi ngati zili chomwecho ndiye siyani ndipita kwa wina."



"Wachedwa mphwanga. Kodi siudziwa kuti mate anga ngachabe? Mnzakoyo ndinena pano wamwalira. Wafa, wapita kumbiya zodooka."

"Nanga ndiye nditani ine? Sindidapitepo kumanda kukafukula mtembo."

"Ayi zonse zimachita kuyamba. Uyamba lero mbale wanga."

"Toto ine ndakana."

"Wati chiyani?"

"Ndikuti ndakana."

"Wakana?"

"Eee! Ndakana."

"Chabwino pita. Kafike bwino. Tidzaonana Chauta, Mphambe, Namalenga akalola. Pita bwino mwanawe, koma dziwa kuti padiwa sasewera. Ukakaona kuti liwombo lasweka pomwe udzikafika kunyumba ndiye kuti akulu akukhoma nkhonya ya chiswambiya."

Wodzasumayo adatuluka nayenda mwamantha. Pomwe ankafika kunyumba kwake adangozindikira kuti wasanduka mkazi. Aphwanga Chipolopolo sadali woti nkusewera naye. Amakhoza kumusintha mwamuna kukhala mkazi, mkazinso amakhoza kumukhalitsa mwamuna.

Anzathu alero ili mungoti ndi bodza lamkunkhuniza, kaya zanu zimenezo. Chipolopolo amakhoza kutembenuza mutu wa munthu. Nkhope kuiphatika kunkhongo, nkhongo kuibweretsa kutsogolo. Ali phee osatekeseka. Mbiri ya Chipolopolo ndi yodziwika bwino. Anthu amachoka ku Sasafirika kudzalandira chithandizo kwa Chipolopolo.

Inu mmati anthu athu adakapulumuka bwanji kunkhondo ya Ajeremani? Dzapiteni ku Keyala mukapezana ndi akuluakulu ndipo akakuuzani za Chipolopolo. Kodi inu mukuyesa kuti poyamba dzina lake lidali Chipolopolo? Dzina lake lenileni lidaali Basikolo

Mwati munthu atafa adadzauka mkango? Zidatani? Kodi adali wokhwima? Nkhani yoopsa iyi. Thupi lonse lingoti zii. Mwachita bwino kuiyambitsa masana, sinkhani ya usiku imeneyi.

Inde wananu ku Mondwe kudali n'ganga yotchuka dzina lake Chipolopolo. Imati ikakwiya nkumuuza munthu kuti dzuwa silimulowera basi ulendo umakhaladi omwewo. Aphwanga Chipolopolo sadali wamasewera. Iye ndiwo amadya mfutso wa nyama ya anthu. Timakanda amangobwira ngati ngumbi.

Chaka china chake Chipolopolo akuti adachita zozizwitsa. Anthu awiri m'mudzimo adakangana chifukwa cha malire a munda. Mmodzi wa iwo adapita kwa Chipolopolo. Lisadalowe dzuwa munthu winayo anali ali kulichete. Nkhani yonse idavutira pamalipiro a ntchitoyi.

"Mmene udzikafika kunyumba mnzakoyo akhala atasiya kupuma," adatero Chipolopolo kwa munthu wodzasumayo.

"Mwagwira ntchito," adayamika wodzasumayo. "Munda umene uja adatisiyira agogo athu. Iye uja ngobwera. Mwandithandiza kwambiri."

"Tsono tikambe za malipiro ake," adatero Chipolopolo.

"Eeee.. Mfumu yanga. Nenani ndibweretse nkhuku zingati?"

"Maliro a mnzakoyo akhala oika mawa," adalongosola Chipolopolo. "Zikatero iwe usiku omwewo kapite kumanda ndifuna ukandibweretsere mtima wake ndidili nawo ntchito."

"Mwati chiyani?" Adafunsa wodzasumayo mwamantha.

"Wamva zomwe ndanena, usandifunse dala. Tiye pita mwamsanga."

"Ayi ngati zili chomwecho ndiye siyani ndipita kwa wina."



"Wachedwa mphwanga. Kodi siudziwa kuti mate anga ngachabe? Mnzakoyo ndinena pano wamwalira. Wafa, wapita kumbiya zodooka."

"Nanga ndiye nditani ine? Sindidapitepo kumanda kukafukula mtembo."

"Ayi zonse zimachita kuyamba. Uyamba lero mbale wanga."

"Toto ine ndakana."

"Wati chiyani?"

"Ndikuti ndakana."

"Wakana?"

"Eee! Ndakana."

"Chabwino pita. Kafike bwino. Tidzaonana Chauta, Mphambe, Namalenga akalola. Pita bwino mwanawe, koma dziwa kuti padiwa sasewera. Ukakaona kuti liwombo lasweka pomwe udzikafika kunyumba ndiye kuti akulu akukhoma nkhonya ya chiswambiya."

Wodzasumayo adatuluka nayenda mwamantha. Pomwe ankafika kunyumba kwake adangozindikira kuti wasanduka mkazi. Aphwanga Chipolopolo sadali woti nkusewera naye. Amakhoza kumusintha mwamuna kukhala mkazi, mkazinso amakhoza kumukhalitsa mwamuna.

Anzathu alero ili mungoti ndi bodza lamkunkhuniza, kaya zanu zimenezo. Chipolopolo amakhoza kutembenuza mutu wa munthu. Nkhope kuiphatika kunkhongo, nkhongo kuibweretsa kutsogolo. Ali phee osatekeseka. Mbiri ya Chipolopolo ndi yodziwika bwino. Anthu amachoka ku Sasafirika kudzalandira chithandizo kwa Chipolopolo.

Inu mmati anthu athu adakapulumuka bwanji kunkhondo ya Ajeremani? Dzapiteni ku Keyala mukapezana ndi akuluakulu ndipo akakuuzani za Chipolopolo. Kodi inu mukuyesa kuti poyamba dzina lake lidali Chipolopolo? Dzina lake lenileni lidaali Basikolo

Wadi Macheso. Ili la Chipolopolo lidayamba nthawi ya nkhondo ya Ajeremani. Achimwene, akuti nkhondo itavuta munthu wina adawauza Ajeremani kuti apite kwa ng'anga yachikuda yomwe idali ndi mankhwala oti chipolopolo kulasa osalowa pathupi la munthu. Ajeremani atapita kumeneko ng'anga Basikolo Wadi Macheso sadalole kuwathandiza. Powakanira chomwecho sindiye Ajeremani kwiyani. Sindiye yambani kuiombera ng'anga. Adaziona ana azungu kumeneko sindiye akuti zozwetetsa mutu.

Akuti achimwene mwana wa mzungu kuima apo ndi kuiphulitsa mfuti, ng'anga yachikudayo kumangoseka. Mfuti yalira koyamba ng'angayo yasanduka buluzi. Khama la mzungu sindiye amvekere ndiombera buluziyo, akatero angoona buluzi wasanduka njoka, kuombera njoka angoona yasanduka khoswe, khoswe wasanduka nsomba, nsomba yasanduka tsache, tsache lasanduka munthu. Uyo munthu ali apoyo, akungomwetulira.

Kumuombera munthu sadzagwa pansi. Kenaka munthu wosafa ndi kuomberedwayu adangoima njoo. Akangotsokomola m'kamwa mwake kutuluka njuchi, ndiyetu njuchi lumani Ajeremani, nkhope zawo tupani. Apatu ndiye pomwe azungu adadziwa kuti munthu wakuda nayenso ali ndi sayansi yake yoipa. Akuti Ajeremani adayesa umu ndi umu kumunyengerera mkuluyo kuti apite naye kwawo, koma adawakanira.

Dzina la Chipolopolo lidayambira pa zoopsa zomwe mkuluyu adawaonetsa asirikali aku Jeremani. Anthu ambiri am'mudzi mwa Mondwe omwe adatengedwa kukamenya nawo nkhondo ya Ajeremani adabwerako ndi moyo. Akuti akazi awo kumudzi m'mawa ndi madzulo ankasamba mankhwala omwe Chipolopolo ankawapatsa, basi akatero amunawo kunkhondoko akaomberedwa m'mfuti za adaniwo mumatuluka madzi okhaokha. Sikutitu onse adapulumuka ayi. Ena adafera



kunkhondoko, koma malinga ndi zikhulupiriro za anthu akuti omwe adafawo nchifukwa chakuti kumudzi akazi awo adanyozera malangizo a Chipolopolo.

Zonsezitu nzomangoti akuti zidatere... akuti zidatere. Akuluakulu olongosola nkhanizi ena akuti adachita kudzionera okha, koma ambiri ndi onena kuti adauzidwa ndi makolo. Chosangalatsa nchakuti ngakhale omwe adachita kumva kuchokera kwa makolo, polongosola nkhanizi sikutsimikiza kwake. Usati uwatsutse pena pake, achita kufuna kukumenya. Iwo polongosola nkhanizi m'maso muli mbee ngati kuti adawaonadi Ajeremani akumuombera Chipolopolo.

Mutu 2

## Imfa ya Ng'anga

Tamvani zomwe zidachitika Chipolopolo atamwalira, atakhwasulakhwasula ana a eni ake, atamezameza nthuli za nyama za anthu, atamwaimwa magazi a anzake kuyesa thobwa, atanyambitira uwende, mwinimoyo adamuitana. Kodi mudamvapo za momwe amafera anthu okhwima? Nzoopsatu. Zoonadi kumanda nkoopsa. Matenda a Chipolopolo adayamba ndi nyamakazi.

Kenaka iyayi m'mimbamu kupota kokhakokha. Patangopita masiku atatu adamva mutu waukulu. Sabata inayo miyendo yazizira, Chipolopolo sakutha kuyenda. Omuyang'anira palibe chifukwa akazi wake adamuthawa kalekale ndipo adakakwatiwanso kwawo. Mwana mmodzi yemwe Chauta adamupatsa adachita kuotchera ngati kamwanapiye. Nkuonatu mkazi adafika poulephera ukwatiwo. Nanga ngakhale nkhuli ndi nkhuliyo ndiye mpakana ndi mwana wako yemwe kutafuna?

Tsopano pa matenda amenewa chithandizo chidali chochokera kwa Abiti Macheso omwe ndi alongo a Chipolopolo. M'mimba mwa mayi wawo adabadwamo awiri basi, Chipolopolo ndi Abiti Macheso. Ukwati wa Abiti Macheso udatha kalekale. Nawonso adabereka mwana mmodzi yekha wamkazi, Biti Joni.

Abiti Macheso adachilowa chintchito choyang'anira matenda a Chipolopolo. Matendawa adatenga nthawi yaitali. Akutitu padafika poyamba kuvunda miyendo koma kumutu kuli gwaa. Akuti kulankhula ndi anthu



amalankhula bwinobwino. Vuto lalikulu lidali fungo lokha basi. Mpakanatu anthu adasiya kumadzazonda matendawo chifukwa chonunkha m'kanyumba amagonako.

Zoopsa zidayamba kuoneka patatsala tsiku limodzi kuti Chipolopolo amwalire. Phiri la Mbamba lomwe lidali loyandikana ndi nyanja ya Maji kalelo linkasunga mikango, koma zonsezo nzakale. Mum'badwo wa a Chipolopolo chidali chinthu chachilendo kumva kubangula kwa mikango m'phiri la Mbamba. Koma tsiku loti Chipolopolo amwalira mawa mikango idzachezera kubangula usiku wonse.

Akutitu Chipolopolo adawauza Abiti Macheso kuti akadzamwalira adzasanduka mkango, ndikuti Abiti Machesowo chonde, chonde asadzayerekeze kuuthamangitsa mkangowo. Nkhaniyitu akutitu idachitikadi kalelo. Akutitu pali zambiri zomwe Abiti Macheso sadaulule kwa anthu.

Chipolopolo atamwalira mtembo wake udasungidwa sabata yathunthu chifukwa choti mtima umaoneka ngati akadali ndi moyo. Maso okhawo ndiwo amaoneka kuti munthuyo wamwaliradi. Ena amanena kuti Chipolopolo adakaikidwa m'manda asadamalizike, koma ena amatsutsa ndipo amanena motsimikiza kuti adakaikidwa ataferatu.

Patapita masiku awiri Chipolopolo ali m'manda akuti kamkango kadatulukira kunyumba ya Abiti Macheso. Tsono poti akuti Abiti Machesowo adali kukayembekezera ndiye sadachite kudabwa nako kachilomboko.

Kamkangoko akuti kamkasungidwa kuchipinda. Chakudya ndi madzi ankakapatsira kuchipinda komweko. M'mudzimo palibe ankadziwa za kamkangoko, koma nthawi zina akuti tiwana todzasewera ndi Biti Joni

mwana wa Abiti Macheso timauza makolo zoti taona mphaka wamkulu titakasewera kwa mnzawoyo.

Nkutheka kodi munthu kumasunga chilombo m'nyumba anthu ena osadziwa m'mudzi? Akuti inde zimatheka. Akuti musalola wina akunamizeni kuti sizingatheke. Si awa Abiti Macheso amasunga kamkango? Amadziwa ndani kuti muli kachilombo m'mudzi wa Mondwe? Palibe ndi mmodzi yemwe amadziwa.

Mkangowo utakula kuchipindako akuti Chipolopolo adawalankhula Abiti Macheso kumaloto, kuwauza kuti autulutse kuchipindako. Ndiye akuti atautulutsa udalowera kunkhalango m'phiri la Mbamba. Anthu adayamba kumva kubangula kwa mkango pakati pausiku. Kenako chipwirikiti. Udayamba kugwira ziweto.

Chilombo chochenjera ngati ichi anthu sadachionepo. Akuti tsiku loti alenje a boma abwera icho zii, osabwera. Tsiku lina amuna adatenga zida zawo ndi kukazungulira phiri la Mbamba, koma ayi adangotaya nthawi pachabe. Sichidzaoneka chilombocho. Alenjewo akabwerera komwe ankakhala ndiye kuti chiweto chijiwa tsiku limenelo. Akutitu tsiku lina mkangowu udadzagwira ng'ombe dzuwa likuswa mtengo. Si za mwawanthu izi? Chodabwitsa nchakuti mkangowu udagwira ng'ombeyo mpakana kuikokera kutchire padalibe ndi mwamuna mmodzi yemwe wolimba mtima. Zida zonse zija zidapita kuti? Akuti amunawo ankangomva m'thupi zii. Eti ankayamba kufuula mkangowo utapita ndi ng'ombeyo.

Ha! Haa! Zitsiru za zimuna. Mwati chiyani? Zitsiru? Mudaidziwa inu mikango ya matsenga? Muli ndi masewera inu eti. Zitsiru? Mumazidziwa zitsiru kuti zimakhala za mtundu wotani?

Kupha mkango wa matsenga nkovuta. Nthungo zimachita kunjanja pathupi pake. Tsonotu



ukavundumuka ndiye nonse chipere. Ngakhale alenje amene akhoza kumangodzigwera okha.

## Kunja Kwaopsa

Anthu adayamba kujiwa. Poyamba adajiwa adali mayi wina pochokera kunkhuni. Sabata yomweyo mkulu wina adajiwa pochokera kumunda. Zonsezi zinkachitika masana okhaokha dzuwa likuswa mtengo.

Poti anthu onse adalephera, mzungu yemwe ndi mlenje wamkulu adangoti zikakhala za matsenga ndi zanu zimenezo. Dzina lake akuti lidali Motimar, koma anthuwo posadziwa katchulidwe ka dzinalo amamutcha Motomayere.

Tsiku lomwe adatulukira mzunguyo m'mudzi wa Mondwe mfuti yake ataberekera pamsana, ana ankamulondola kulikonse komwe amayenda akumamuyamikira.

*Motomayere wabwera kudzapha mkango.*
*Motomayere ndi mwamuna wogona kukhomo kusat-seka.*
*Motomayere mlenje wamkulu.*

Madzulo Motomayere ndi anyamata ake adasonkhana pansi pa chimtengo chachikulu pomwe adamanga matenti. Mzunguyo ankamwa mowa wake wa m'mabotolo. Anthu ankanena kuti amamwera dala mowawo chifukwa umachotsa mantha. Izi nzonena za anthu osati iye mwini Motomayere.

Chenjezo kwa aliyense m'mudzimo lidali lakuti usiku palibe wotuluka kunja. Tsono anthu anadya mwamsanga patsikulo nkudzitsekera m'nyumba zawo. Kunja kutagwa mdima Motomayere adayamba kuzungulira mmudzimo.



Posakhalitsa adangoona kufiira kwa maso ndipo adadziwa kuti mkango uja ndi umenewo. Nthawi yomweyo Motomayere adachalira bwinobwino nkuiphulitsa mfuti. Sadaphonye. Adangoswerat u mutu wamkangowo. Anyamata ake adafuula kudziwitsa anthu kuti chilombo chija chaphedwa.

Anthu adatuluka m'nyumba zawo akuthamanga. Amayi thungululu zili m'kamwa. Zoonadi ndithu kuti azungu saopa za matsenga. Si uyu Motomayere walasa chilombo chomwe chidavutitsa m'mudzi wa Mondwe.

Enatu sankakhulupirira konse kuti Motomayere waphadi chilombocho. Iwo amati pofika m'mawa mkangowo ukhala utadzuka. Koma kuti? Bodza limenelo. M'mawa kutacha adachipeza chilombo chija chili gone.

Tsono tamvani zomwe zidachitika patsikulo. Abiti Macheso akuti adabwera akuthamanga akulira ngati kuti wafayo ndi munthu:

"Achimwene mwafa kawiri kalanga ine! Achimwene mwafa kawiri. Nditsala ndi yani ine! Mayo ine!"

Nthawi yomweyo gulu la anthu lidawagwira Abiti Macheso nkuyamba kuwamenya. Kani zomwe zinkamveka kuti mayiyu ankasunga chilombo m'nyumba nzoona eti? Mthakati, mfiti, mdyawanthu wachabechabe.

Motomayere manja pakamwa. Wadabwa mwana wa mzungu. Nanganso nchiyani ichi? Akuti mayiyu ankasunga chilombo m'nyumba? Ndiye zaka zonsezi chilombocho osaonekera kunja? Zabodza izi. Mulekeni munthu wosalakwa. Ndikuti mulekeni. Waitulutsa mfuti Motomayere. Anthu onse balala kuwasiya Abiti Macheso ali pansi kwalaa.

Aka sikoyamba mwana wa mzunguyu kumva zikhulupiriro za anthu akuda. Zaka zapitazo Motomayere adaona nkhalamba ina ikumenyedwa chifukwa chakuti eti inkamanga mvula. Kwa mzungu izi nzoseketsa.

Kumanga mvula? Munthu angamange mvula? Angaimange nchiyani?

Kalanga ine, umbuli wa azungu. Sadziwa sayansi ya anthu akuda. Sadziwa kuti pomwe iwo azungu ali kalikiliki kuulula ufiti wawo anzawo anthu akuda ali phee, angoti mawa lino tiona wochenjera. Kukada munthu wakuda angokwera pa chiphapha cha lichero kuuluka kupita ku Sasafirika. Savutika za chitupa choyendera, sadandaula za chikalata cha katemera wa Kolera kapena nthomba.

Motomayere iwe usawaikire kumbuyo Abiti Macheso. Ankasunga chilombo m'nyumba mwawo amenewo. Kodi udalowako kuchipinda kwawo? Chipolopolo adawasiyira zambiri. Aleke anthu akonze. Mwina akadzafa okha nawo adzasanduka mkango. Leka ndiwe wobwera, usalowerere za eni ake, upwetekedwa.

Madzulo a tsiku limenelo Motomayere ndi anyamata ake adamasula matenti awo ndi kubwerera kumaofesi awo. M'mbuyo muno anthu adawagwiranso Abiti Macheso nkuwamenya kodetsa nkhawa. Mwana wawo Abiti Joni adawatengera kuchipatala komwe adangokakhalako masiku awiri nkumwalira. Mtembo utabweretsedwa kumudziko anthu ochepa achisoni adakawaika m'manda. Imfa ya Abiti Macheso idali yomvetsa chisoni. Kaya nzoonadi kuti ankasunga mkango, nkovuta kuti munthu pawekha utsimikize, koma nkhani yake ndi yoti anthu akuti zidali chomwecho.

Nkhani yovuta iyi. Kodi Chipolopolo adalipodi kapena nzopeka chabe? Kaya inu, koma akuti adalipo ndithu, anthu adamuonadi. Nanga Motomayere, Abiti Macheso ndi Biti Joni, kodi adalipo kapena zonsezi nzam'mutu chabe?

Kaya inu, komatu ena akuti adachita kuwaona. Pambuyo pake Motomayere adabwerera kwawo ku Mangalande. Abiti Macheso pajatu adamwalira. Biti Joni



ndiye alipo wamoyo mpaka lero lino. Tikamba pano ali ku ndende. Biti John ali ku ndende? Eee! ali kundende. Nayenso adapalamula chiyani? Nkhani yake nkukhala ya malume wake kapena amake Abiti Macheso? Ayi sizimenezo. Izo kodi sizakalekale. Sizimenezo. Nayenso ali ndi zake. Chachikulu choti mudziwe nchakuti Biti Joni alipo koma akusewenza kundende. Kalanga ine Biti Joni, kubala kwa Abiti Macheso, tsoka silidakuchokere iwe mpaka lero? Biti Joni, Biti Joni.

Mutu 4

## Kunsi kwa Mulatho

Mwana wamasiye Biti Joni. Atate wake sawadziwa. Adathawa kalekale. Amake Abiti Macheso ndiye awa adafa nkumenyedwa pa nkhani ya ufiti. Biti Joni adatsala yekha. Anthu m'mudzimo kumangomuthawa. Kusewera osamasewera ndi kamwana kamkango. Kupusa nako kakhoza kukutafunira mwana iwe utapita kuchitsime kukatunga madzi. Biti Joni ndi kamwana ka mfiti. Aliyense amangokathawa.

Mavuto kwa Biti Joni kukula kwake ngati kamwanapiye kongoti kubadwa lero basi nthawi yomweyo kuyambapo kutoleza chakudya. Momwemodi Biti Joni, kudya amachita kuti lero adya kunyumba iyi, mawa athamangira kwina, nkucha agonapo ndi njala.

Atakula Abiti Joni adaganiza zopita kutauni. Adayenda pansi mitunda zana limodzi. Ulendowu ndi wokafuna ntchito yolera ana. Wina adawalumapo khutu Abiti Joni kuti kutauni akhoza kukapeza ntchito kwa amwenye, azungu kapena anthu akuda odya bwino.

Ulendo wodetsa nkhawa uwu. Abiti Joni sadziwako munthu aliyense kutauni. Chomwecho vuto loyamba ndi malo ofikira. Adalibe chakudya, bulangete ndiponso zovala zake zidali sanza zokhazokha. M'njiramu ankakhalira kupempha. Anthutu ndi okoma mtima kunja kuno. Amawapatsako Abiti Joni chakudya ndi madzi. Ambiri amaganizira kuti mayiyu ndi wamisala kapena wopemphapempha.



Atafika kutauni Abiti Joni adasowa kolowera. Iyi idali nyengo yozizira kwambiri. Mwayi kuti masiku amenewo kudalibe galimoto zambiri. Likadakhala lero Abiti Joni akadaombedwa pooloka misewu.

Dzuwa litatsala pang'ono kulowa Abiti Joni adaona anthu ovala sanza atasonkhana pansi pa mulatho. Adapita pafupi ndipo adapezapo anthu akhungu, opuwala ziwalo ndi ena abwinobwino.

Mayi wina wopuwala dzanja adawalonjera Abiti Joni, "Tikuthandizeni?"

"Eee... ndine Biti Joni. Ndine mlendo. Ndikufuna malo ogona."

"Mwachokera kuti?"

"Ku Mondwe."

"Ndiye kuti kumeneko."

"Kudera la nyanja ya Maji?"

"Ayi musavutike kulongosola sindingakudziwe. Tsono kuno mwabwerera zathu zomwezi ngati?"

"Zanu zomwezi?" Adafunsa Abiti Joni modabwa.

"Eee zathu zomwezi."

"Ziti?"

"Zopemphapempha, umasikini."

"Ayi, ine siwopemphapempha. Ndingofuna malo oti ndigonepo lero," adalongosola Abiti Joni.

"Ndiyetu pepani mwafika kumalo olakwika. Kuno sikunyumba yogona alendo. Kuno nkokhala amasikini. Ife anthu opemphapempha."

"Kodi nkutheka kuti ndigone nawo kuno?"

"Palibe vuto, koma nanga inu simwati mukufuna kogona alendo."

"Ayi sindidatero, simudandimve bwino. Munthune ndilibe mnansi kutauni kuno, ndalamanso ndilibe."

"Chabwino bwerani mundilondole."

Abiti Joni adamulondola mayi wopuwala dzanjayo. Pansi pa mulathowu padali chifungo cha matayala a

galimoto omwe anthuwo amaotha. Tiwana tamasikini timathamangitsana ndi kumachita masewera obisalirana.

Amayiwa adafika pa kanyumba kamakatoni kumathero kwenikweni kwa mulathowu. Ataodira mayi opuwala dzanjayo mwamuna wakhungu adatuluka.

"Ndabwera ndi alendo," adatero mayi opuwalayo.

"Zikomo, mayi wanga," mkulu wakhungu uja adawalandira. Khalani pa chipepala cha pulasitikicho."

"Zikomo ... Zikomo," adathokoza amayi awiriwo nakhala pansi.

"Eee! Mwatiyenderatu alendo?"

"Awa ndi alendo," adalongosola mayi wopuwalayo. "Dzina lawo ndi Biti aa.. paja Biti ndani?"

"Ndine Biti Joni."

"Kubweraku akufuna malo ogona. Akuti achokera kutali ndipo kutauni kuno alibe mbale aliyense. Tsono Abiti Joni, awa ndi a mfumu athu kuno kunsi kwa mulatho. Dzina lawo ndi a Kwapsankungala, koma eni ake timawatcha a mfumu. Ndiye ine ndikusiyeni." Mayi wopuwalayo adanyamuka napita kumalo ake ogona.





## Malo Ogona

Mkulu wakhunguyo adatsira fodya wake wamfuno padzanja lakumanzere ndi kunkokera yenseyo mfuno. Atatero adayetsemula. Amati akayetsemula kuchita kumveka kunsi kwa mulatho konseko. Aliyense amadziwa kuti mfumu yanunsira fodya wake.

"Pepanitu mayi ife ndife akhungu. Chomwecho sititha kukuthirani m'maso."

"Ayi musadandaule izo zilibe kanthu."

" Tsono akuti ndinu alendo, mwachokera kuti?"

"Kwathu ndi ku Mondwe kunyanja ya Maji."

"Kuno mwafika liti?"

"Mukati kuno munena kunsi kwa mulatho kuno?"

"Ayi, ndinena kuno kutauni."

"Ndafika lero. Kwathu nkutali. Ulendo wanditengera masiku asanu. Ndilibe mbale. Ino ndi nthawi yanga yoyamba kubwera kuno kutauni."

"Chakubweretsani kutauni kuno nchiyani? Kudzafuna ntchito kapena kudzapempha?"

"Kudzafuna ntchito. Pofunafuna malo ogona ndidaona kunsi kwa mulatho kuno kuli anthu, nchifukwa chake ndabwera kuti ndipeze nawo malo."

"Mayi muli apa, kuno kunsi kwa mulatho ndi kwa ife anthu opemphapempha, amasikini opanda kwawo, odya za m'mabini. Kodi mabini mumawadziwa?"

"Ayi sindidalimvepo. Mabini ndi chiyani mfumu?"

"Mabini?"

"Eee mabini, liwu loti mabini mudayamba mwalimvapo chibadwire chanu?" Adafunsa mfumuyo, nabwereza liwulo motsitsa mawu kawiri, "mabini... mabini."

"Nanga chitini kapena chibekete mumachidziwa?"

"Eee ndimachidziwa."

"Mabini ndi zitini kapena zibekete zomwe amwenye, azungu ndi anthu akuda odya bwino amatayiramo zinthu zomwe alibe nazo ntchito m'nyumba zawo. Zinthu monga sanza, mikute ndi mafupa a nyama. Mumapezeka zikolopa, izo ife timatola chifukwa kwa ife zimenezo ndi zovala; mikute ya dzana, kwa ife iyo ndi nsima yamoto; mafupa a nkhuku ndi minga za nsomba, izo kwa ife ndi ndiwo za nkhuli, tikazipeza timachita kukanganirana ngati tapeza nyama yoti yangochokera m'serempani. Tikachita kupeza ziboda za nkhukuzo dovu limachita kudontha doo-doo! Mukakhala m'mabini mwa a mwenye nthawi zambiri timapezamo mpunga. Mwinatu timachita kudabwa ndi kuchuluka kwa mpunga wotayidwa m'mabiniwo, kudabwatu kuti kodi adachita kudzataya mphika wathunthu? Kuchuluka kumeneko. Koma mpungawo umakhala woti ndi wa dzana ndipo waonongeka. Kwa ife ndi phwando lalikulu limenelo."

Chifukwa cholankhula mopitiriza mkuluyo adatsamwa ndi mate. Abiti Joni adangokhala mokhumata. Sankamvetsa kuti cholinga cha mfumuyo polankhula zonsezo nchiyani? Abiti Joni adali atatopa ndipo ankafunitsitsa atapatsidwa malo oti agonepo basi.

"Malo ogona alipo tikupatsani. Anthu angapo osowa kokhala tawasungapo pano pansi pa mulatho. Vuto la anthu inu ndi ili - mukapeza tintchito tanu tolera ana m'masitolomu, basi m'maiwala malo omwe mudapumitsira nthiti tsiku lanu loyamba kutauni kuno. Ena mabwana anu akakutumani kukagula zinthu kumsika m'madutsa umu. Ine ndilibe maso, koma



anzanga a maso amakuonani ndipo amandiuza umo mmati ponyogodola. Nthawi zinatu ndimaseka ndekha kuti kodi ntchito zolera anazo mumalandira tindalama tingati K5 basi? Ife anzanu kukatichera bwino tikampanikiza mzungu amakhoza kutigwetsera K10. Chachikulu ndicho kumpanikiza mzunguyo. Akati adutse msewu uli naye. Akalowa m'sitolo iwe kumudikira panjapo. Akatuluka uli naye mpakana pa galimoto yake. Tsono amatopa basi amangochitulutsa chimpukutu nkukupatsako K10. Ayi musadandaule Abiti Joni malo ogona mwawapeza. Kaya chakudya mwadya kale ngati?"

"Ayi sindinadye."

Mkuluyo adapisa m'thumba lake la chiguduli nkutulutsamo buledi wouma kwambiri nkuwapatsa Abiti Joni. Iwo adalandira mkute wa bulediwo ndi kuyamba kuudya. Mkulu uja adaima mothandizika ndi ndodo yake ya msungwi.

"Sikeletoni! Sikeletoni!" adaitana mkuluyo.

"Wawa!" Kadaitanika kanyamata kowonda ngati sikeletoni.

"Uwatenge mayiwa, dzina lawo ndi Abiti Joni, upite nawo kwa Anasumbulera awapatse malo ogona. Uwauze kuti akhala kuno kunsi kwa mulatho kufikira atadzapeza kwina kokhala."

"Zikomo ndamva wawa."

"Pitani ndi mwanayu mayi."

"Ndathokoza mfumu," adatero Abiti Joni. Adanyamuka napita ndi mwanayo.

Atafika kwa Anasumbulera mwanayo adawasiya. Anasumbulera adali mayi wachikulire ndithu. Wooneka wathanzi. Wopanda chilema chilichonse. Nawonso chifukwa chokhalitsa kunsi kwa mulathoku amasikini ambiri amawapatsa ulemu. Mayiyu amagwira ntchito yaikulu ya uzamba. Ana onse amene adali kunsi kwa mulathoku adabadwira m'manja mwa Anasumbulera.

Iwowa sankapita nawo komakapempha. Kwawo kudali kungokhala basi, koma madzulo aliyense amabwera ndi kangachepe. Nthawi zambiri Anasumbulera ankapita kuganyu yosinja kumalaini.

Abiti Joni adapeza ufulu ndithu. Anasumbulera adawapatsa Abiti Joni ziguduli zoti afunde. Tsiku limeneli kunazizira kwambiri kotero kuti amasikini adakhala m'timagulutimagulu kumaotha moto wa matayala. Amayi awiriwa asadagone adacheza kwanthawi yaitali ndithu. Abiti Joni adauza Anasumbulera za mavuto awo onse. Anasumbulera nawo adalongosola za momwe adabwerera m'taunimo zaka zambiri zapitazo.

"Zaka zonsezi mwakhala muli pansi pa mulatho pano?" Adafunsa Abiti Joni.

"Eee zaka zonsezi ndithu. Anthu andipeza ndipo andisiya pano. Ana abadwa, kukula, kukwatira kapena kukwatiwa ndikuwaona pano."

"Kani pamakhalanso zikwati pansi pa mulatho pano?"

"Eee zimakhalapo. Inu mmati sizikhalapo. Amasikiniwo alibe chiyani? Timamangitsa zikwati ndipo zimalimba ndithu. Ana ena akakula amathawa nkumakakhala kwa okha."

"Koma kuzizira kumeneku ana akhandawa ndiye bwanji?"

"Chiyani?"

"Ndinena kuzizira kumeneku zibayo bwanji?"

"Aaa inu mudandaula zibayo. Ana a kunsi kwa mulatho safa wamba. Matupi awo ndi okhwima. Zaka zonse zimene ndakhala kuno maliro a ana chifukwa cha matenda a chibayo ndi ochepa kwambiri."

"Tsono Anasumbulera nditakufunsani funso limodzi."

"Funsani."

"Kodi ntchito nkwapafupi kuipeza kutauni kuno."

"Kani mwabwera kudzafuna ntchito?"



"Eee ndabwerera ntchito."

"Ntchito ya mtundu wanji?"

"Iliyonse. Kaya ndi yolera ana. Iliyonse."

"Koma mmene mulirimu ndiye nkovuta. Usiwa muli nawowu nkovuta kuti munthu akulembeni ntchito. Langizo langa nlakuti muyambe yomakasinja m'malainimu. Mutapeza ndalama basi mukagule zovala zabwino. Mukadzatero pambuyo pake mukhoza kuyamba kufunafuna ntchito yabwino."

"Zikomo kwambiri mwandipatsa nzeru."

"Ndisanaiwale, ndikuchenjezeni kuti usiku musayerekeze kupita kutali ndi malo anu ogona. Mukafuna kudzithandiza kungoimirira cha pafupi pomwepa. Anyamata omwe apita koyenda usiku amakhala akubwerako pakati pa usiku."

"Anyamata akunsi kwa mulatho kuno amapita koyenda usiku?" Anadabwa Abiti Joni.

"Eee ambiri amati akapemphetsapemphetsa amapita kudansi kukavina usiku. Tsono akamabwerako amakhala ataledzera."

Abiti Joni adatsala pang'onong'ono kuseka.

"Nawo opempha amakhala ndi maganizo opita kudansi kukasangalala. Zoseketsa. Basi masana akatoleratolera, madzulo nkuvula sanza zawo zija nkuvala zovala zabwino. Koma tanenani bwino kudansi kwake kuti angakawalowetse anthu opempha, amasikini? Ndimayesa kuti kovinira madansi m'tauni muno chilankhulo chake ndi Chingerezi ndiye zimawathera bwanji?"

"Aaa inu, limenelo ndi vuto? Chingerezitu sichilankhulo chovuta. Simalinga kudziwa kunena *Yesi* ndi *no* basi. Chachikulu nkukhala ndi ndalama yolowera pakhomo."

Pakati pa usiku anyamatawo adatulukira ndi chiphokoso chawo. Mpakanatu mfumu ya kunsi kwa mulatho ija idadzuka nkuwakalipira.



Mutu 6

## Ganyu Yosinja

Mmawa Anasumbulera adauza Abiti Joni kuti akhoza kupitira limodzi kumalaini kukagwira ganyu yosinja. Anasumbulera adali mayi wodziwika kumalaini chifukwa amati akati wagwira munsi ndiye kuti posakhalitsa amaliza mitondo itatu. Amakhoza tsiku limodzi kusinja kunyumba zisanu.

Chomwecho Abiti Joni adaphunzira kulimbikira pa ganyu yosinjayi. Amati akasinjasinja madzulo nkubwerera kunsi kwa mulatho kuja. Anasumbulera adauza Abiti Joni kuti ntchito yosinja ndi yabwino kuposa yolera ana. Malipiro a amayi olera ana ndi K5 pamwezi pamene yosinja munthu akakhala wamphamvu ndalama yomweyo akhoza kuipeza pa sabata imodzi yokha.

Abiti Joni adaona kuti ndi bwino kudalira ganyu yosinja nkumakhala nawo kunsi kwa mulatho. Kwanthawi yochepa monga ena onse okhala kunsi kwa mulathoko nawo Abiti Joni adakatola makatoni ndi mapulasitiki nkumanga kanyumba kawo. Zokafuna ntchito yolera ana padalibenso.

Zinthu zochitika kunsi kwa mulatho nzambiri. Anthu okhala kumeneko siopusa, ndi anzeru zodabwitsa. Gulu loyamba ndi la akhungu. Ambiri a iwo adabwera kutauni kalekale. Munthu ukhoza kufika m'tauni kudzafuna ntchito nkuipeza nkugwira zaka makumi awiri, nkupuma ntchitoyo, kubwerera kumudzi, akhunguwa oti udawapeza pomwe unkadzafunsira ntchito umadzawasiya utakalamba. Iwo kwawo nkuyendayenda

m'tauni kuti anthu achisoni adziwaponyerako tindalama. Moyo wawo ndi umenewo. Umu ndi momwe Chauta amawasungira.

Gulu lachiwiri ndi la opuwala ziwalo. Nawonso amadalira anthu achisoni, chimodzimodzi monga akhungu aja. Ndiye pali ena onga Abiti Joni. Iwo adathawa mavuto kumudzi, tsono posowa malo okhala m'tauni basi nkungokadziponya kunsi kwa mulatho. Anthu ena powaona awaganizira kuti ndi amisala kapena opemphapempha. Ayi amenewa sadalira m'thumba mwa wina aliyense. Iwo amakadzigwirira timaganyu monga kusinja kapena kulima m'madimba mwa anthu. Nchifukwa chake kunsi kwa mulatho kuli anthu anzeru bwinobwino, zochitika zawo kumeneko ndi zolongosoka ndithu. Tsiku la sabata nawo anthu akumeneko amapembedza Mulungu. Kuli alaliki osiyanasiyana. Ngakhale maukwati awo amamangitsa monga momwe achitira anthu ena onse. Kumakhala maphwando kumeneku ndipo simungakhulupirire mutawaona amasikini mabotolo a kachasu ali m'manja. Anthu odutsa powaona amangoti amisala akondwanji lero? Akondwanji? Anzanu ali pachikondwerero, kudya, kumwa ndi kuvina.

Pakutitu anthuwa ngosaphunzira zawo zambiri amangoloweza. Ndime za m'Baibulo ndi nyimbo sivuto kwa iwo. Amangolakatula ngati ndakatulo. Chimodzimodzi tianyamata tomwe timapita kumadansi natonso tikati tiyimbe nyimbo za malekodi m'Chingerezi, mwati nkutidziwa kuti sitidapondepo m'kalasi.

Abiti Joni adakhazikika kutauni. Malo okhala ndi kunsi kwa mulatho komweko. zobwerera kumudzi adaziyiwaliratu. Masiku nkumapita, zaka nkumatha. Kenaka anthu adangoona kuti Abiti Joni ali ndi pakati. Zataninso nanga? Kuwafunsa Abiti Joni mwini pakatipo sadzamuulula konse. Mpakanatu mwana kubadwa.



Kakongolerenji kamwana kakakazi. Kudalitu chindimba kunsi kwa mulatho tsiku lobadwa mwanayo. Kupereka dzina anthu ankachita kulimbirana. Pamathero pake adagwirizana kuti dzina la mwanayo likhale Zione. Nanga poti amake adakana kuulula mwamuna adawapatsa mwanayo? Onse adati basi adzingoitanikira la amake lomwelo loti Joni. Chomwecho mwanayo ankatchedwa Zione Joni.

Zione adali mwana wosiyana ndi ana ambiri kunsi kwa mulathoko. Mayi wake ankamusunga bwino. Ankavala ngati mwana wa munthu woti ali pantchito yabwino. Atakula Abiti Joni ankamuletsa mwanayo kuti asamapite ndi anzake kopempha m'taunimo.

Kudalinso anthu ena kunsi kwa mulathoku omwe amalera ana awo bwino. Ana oti akamayenda m'taunimu simungawadziwe kuti ndi ana amasikini. Vuto ndi lakuti awa ndi ana omangokula, mwayi wopita kusukulu alibe.

Zione adakulira limodzi ndi atsikana ena awiri Aida ndi Leleni. Makolo a Aida adali akhungu pamene a Leleni adali opuwala miyendo ndi manja. Ana aakazi ovala bwino. Akamayenda apo amuna kumatembenuza mitu kangapo kufuna kuona ziphadzuwa.

Tsiku lina pocheza atsikana atatuwa adakambirana zakuti ndi bwino achokeko kunsi kwa mulatho. Ayambepo kufuna ntchito m'malaini.

"Anzanga ifetu kumeneku ndi kukula," adatero Zione. "Kodi sibwino kuti tsopano nafe tikafune ntchito kuti tizidzithandiza tokha?"

"Ukunena zoona Zione," adayankha Aida. "Tiyeni tiyambepo kufuna ntchito kuti tichokeko kunsi kwa mulatho kuno."

"Kodi anzanga mungoti ntchito, ntchito yake ya mtundu wanji?" Adafunsa Leleni.

"Ntchito iliyonse. Kaya ndi yosinja, yolera ana, iliyonse," adatero Zione.

"He dee!" adaseka Aida. "Yosinja yokha ndiye tisadzinamize; tiyeni tidzikambirana za ntchito yolera ana."

Atakambirana ndi makolo awo onse adaiona kuti nkhaniyi ndi yanzeru. Umu ndi momwe Zione, Aida ndi Leleni adayambira kuyendayenda kumakafuna ntchito ku masitolo a amwenye ndi kumalaini. Atsikana onsewa anabadwa chaka chimodzi, kungosiyana miyezi yokha basi. Mmene amaganizira zomakafunafuna ntchito nkuti ali achikulireko ndithu. Akulu amati otha msinkhu.

Chaka chidawathera atsikanawo osaipeza ntchito. Adazungulira tauni yonse, koma mwayi padalibe. Tsiku lina akudutsa pa bawa ya "Osauka Satopa" mkulu wina adawakodola. Iyeyu adali mwini malo ogulitsira mowawo dzina lake Chimwa Mowa. Dzinali adapatsidwa ndi anthu kutauni komweko chifukwa akuti ngakhale asadatsekule bizinesi ya bawayi anthu ankamudziwa bwino kuti ndi chidakwa. Pa bawa ya "Osauka Satopa" padali pali zii, kuoneka ngati malowa adawatseka. Atsikana atatuwa atafika pafupi a Chimwa Mowa adawafunsa komwe ankapita.

"Tikufuna ntchito," adayankha Zione.

"Ooo! Zayenda bwino. Ine ndikufuna atsikana ogulitsa mowa m'bawamu. Iyi ndi ntchito yofunika atsikana okongola ngati inu. Mukuti chiyani pamenepa? Mtengo wake ndi wabwino," adatero a Chimwa Mowa uku akusuta paipi yawo.

Atsikanawo adapempha kuti akafunse makolo awo poyamba ndi kuti adzabwera mawa lakelo kudzagwirizana bwino ndi eni bawayo.





## Osauka Satopa

Makolo a atsikanawa atauzidwa kuti anawo adapeza ntchito adasangalala kwambiri. Tsopano chithandizo chidzakhalapo chambiri. Nanga iyi sintchito ya pa mwezi? Ukatha azidzalandira malipiro awo.

Zione, Aida ndi Leleni adachita kulawirira mmamawa a Chimwa Mowa asanadzuke. Adangokhala pakhonde pa "Osauka Satopa Bawa" mpaka eni ake adatulukira.

"Ooo! Atsikana mwabwera, lowani, lowani, tikambirane za ntchitoyi. Ndinudi okhulupirika. Ine ndimangoti simubwera," adatero a Chimwa Mowa.

Atalowa m'katimo atsikanawo adakhala pa chidesiki cha thabwa pomwe eni ake adakhala pakauntala. M'bawamu munkangooneka ngati mu bwinja. Mudali timabotolo towerengeka ta Fanta. M'mabotolo a mowa mudalibe chilichonse. A Chimwa Mowa adatsokomola ndi kuyamba kulankhula motsika mawu, "Atsikana, paja maina anu ndinu ndani?"

"Ndine Zione Joni."

"Ndine Aida Njinga."

"Ndine Leleni Sadulo."

"Kodi mudagwirapo ntchito ya m'bawa?"

"Ayi sitidagwirepo," onse adayankha.

"Musadandaule njosavuta. Nanga kuvina kodi mmatha?"

"Aaa, eee kuvina timadziwa. Sivuto limenelo," adatero Leleni.

"Ndiye kuti ntchito mwaipeza," adatero a Chimwa Mowa. "Tsopano ngati zili choncho ndifuna ndikuuzeni za malo ano. Bizinesi yanga ya bawa ngakhale ili chomwechi sikuti idatha ayi. Miyezi itatu yapitayo atsikana ogwira ntchito pano adaphana. Ankalimbirana mwamuna mpaka kudyetsana poyizoni. Mtsikana wodyetsedwayo adakamwalirira kuchipatala ndipo apolisi adabwera pano kudzatitenga tonse. Ine ndatulukako sabata yathayi. Andipatsa chilolezo choti ndikhoza kupitiriza bizinesi yangayi. Ichi ndi chifukwa chake mukuona m'bawa muno muli chomwechi. Pali vuto lomwe sindifuna kukubisirani. Ili nlakuti atsikana ambiri tsopano akuopa kulowa ntchito pano chifukwa cha zomwe zidachitikazi. Tsono pakuti ine sindifuna kukakamiza munthu aliyense ndiyamba ndakusiyani kuti mukambirane ndipo mundiuze ngati ndinu okonzeka kuyamba ntchito imeneyi." Adatuluka panja kuwasiya atsikanawo m'bawamo.

Kwanthawi yaitali atsikanawo adangokhala duu akumangoyang'anana chokamba kusowa. Ntchitoyi amaifunadi, koma zoti atsikana adaphanazi ndiye zoopsa.

"Anzanga mukuganiza bwanji?" Adafunsa Zione.

"Tiyeni tilowe ntchitoyi. Mwayi wathu ndi womwewu tsono tisautaye," adatero Leleni. "Kaya Aida ukuti chiyani pa nkhaniyi?"

"Ndikugwirizana nawe zoti tisaope, tiyambe ntchitoyi. Kaya iwe Zione maganizo ako ndi otani?"

"Ayi ndili nanu anzanga, tiyeni tilowe ntchito. Izi zoti atsikana adaphana pano ife sizitikhudza."

A Chimwa Mowa atalowanso m'bawamo atsikanawo adawauza kuti atakambirana agwirizana zoti ayambe ntchitoyo, osaopa zomwe zidachitikazo.

"Malipiro," adanena a Chimwa Mowa ndi mawu okweza. "Malipiro anu ndi K30 pamwezi aliyense. Anzanu omwe achokawa ndinkawalipira K15, tsono



mukhoza kuona nokha kuti ndakuonjezerani ndalama zambiri. Nyumba zogona zili kuseriku, aliyense ali ndi kachipinda kake. Mabedi ndi zofunda zilipo. Mapoto, miphika ndi mbale ndi za anzanu koma mukhoza kumagwiritsira ntchito chifukwa zoti atuluka posachedwapa kupolisiku nzokaikitsa. Lero palibe zambiri zochita. Galimoto yodzasiya mowa ibwera madzulo. Poyamba ndikuonetsani zipinda zanu ndipo kenaka mukonzekonze m'bawamu kuti muonekenso bwino." Atawaonetsa zipindazo atsikanawo adayambapo ntchito. Adasesa ponsepo, kukolopa ndi kupukuta magalasi a m'mazenera. Madzulo galimoto yodzasiya mowa idabwera ndi zakumwa zamitundu yosiyanasiyana.

Pamene linkalowa dzuwa zofunikira zonse zidali zilipo ndithu.

"Tsono bwerani apa nonse," Chimwa Mowa adawayitana atsikanawo. "Kodi mwabwera ndi zovala zanu zonse."

"Eee tabwera nazo."

"Nanga sopo, mafuta onunkhira muli nazo?"

"Ayi tilibe."

"Chabwino lero sopo ndi mafuta ndikupatsani, koma kuyambira mawa mudzayenera kumadzigulira."

"Mawa lomweli?" Anadabwa Leleni.

"Eee mawali."

"Ndalama zake tizitenga kuti?"

"Atsikana ogwira ntchito m'bawa amakhala ndi ndalama nthawi zonse."

Atsikana am'bawa samapsa. Chachikulu ndicho kuwalandira bwino amuna odzagula mowa. Kuvina nawo bwino. Kuwasowetsera kuseriku. Basi mukatero makwacha amangolakatika okha. Komwe achokera osadziwika bwino. Ngati mufuna kupha makwacha chotsani manyazi ndi kuwaika kutali. Ntchito ya muno

siifuna atsikana opusa, koma ochenjera okhaokha. Pitani mukakonzeke mwamsanga."

Posakhalitsa anthu adangoona magetsi ali waliwali m'bawa ya "Osauka Satopa." Akati asuzumiremo angoona atsikana akuvina. Choimbira chili pamwamba, aliyense m'deralo kudziwiratu kuti a Chimwa Mowa adzukiriranso. Pang'onopang'ono anthu adayamba kubwera. Kenaka awo a galimoto zawo atulukira. Fodya ali pakamwa. Ana aamuna amenewo. Ena obwera ndi tatsikana topaka zofiira m'milomo. Tikamayenda mbina kumachita kugwedera ngati tikusinthira magiya.

"Yesi Chimwa Mowa," adawalonjera mnyamata wina.

"Aaa! Mphwanga ulipo?" Adayankha Chimwa Mowa.

"Ndilipo madala. Inu mumati ndidafa?"

"Ha..Haa..Haa! Kufa mphwanga, ayi. Nanga mmene ndidatsekamu sibasi anthu ambiri osawaona."

"Kodi nkhani ija yatha."

"Kwa ine yatha, atsikana okhawo ndiye akadaali komweko."

"Koma inu ndiye yatha, mulibe mlandu?"

"Ndilibe mlandu mphwanga sukuona kuti zinthu zabwerera mwakale mommuja?"

"Yesi. Chimwa Mowa."

"Yaa! Mphwanga —ha —haaa—-ha! Ukunenepatu. Ukudya zonona et?"

"Ndani? Ineyo? Kudya zonona? Chokani apa a Chimwa Mowa," adatero mnyamatayo ndipo adasunthira pafupi ndi kulankhula monong'ona akuponya maso komwe kudakhalira atsikanawo. "Kodi ndiye tizitete tatsopano?"

Chimwa Mowa adangoyankha ndi mutu. Ngakhale kuti iyi idali nthawi yoyamba kugwira ntchito ya m'bawa, atsikanawo adaoneka amsangala kwambiri. Tsiku limeneli malonda adayenda bwino pang'ono chifukwa choti anthu ambiri sankadziwa kuti "Osauka Satopa Bawa" yatsekulidwanso.



Asanagone atsikanawo adasonkhana m'chipinda cha Zione. Nkhani zawo zidali za ntchito yatsopanoyi.

"Zinthu zikuoneka ngati tayamba bwino," adatero Leleni.

"Ayi apa ndi pomwe timafuna," Aida ameneyo. "Kaya Zione wapeza ndalama zingati?"

"Mkulu ndimacheza naye uja wandigwetsera K5," adanena monyadira Zione. "Nanga pakutha pamwezi ndiye bwanji? N'pabwino pamenepa. Chifukwa tangoganizani atsikana kuti ndalama zimene adzitipatsa amunawa ndi zathu zimenezo, kuwonjezera apo malipiro athu a K30 pamwezi."

"Pabwinodi pano. Tiyeni tikhazikike," adatero Leleni.

## Chikondi cha Kumowa

Pamene unkatha mwezi umenewo pa "Osauka Satopa Bawa" padali patabwerera mwakale muja. Amuna ankayamikira kukongola kwa atsikana atsopanowa. Nawonso amati akasamba nkuvala madiresi atsopano, pamalopo kumagwedezeka ndithu. Amuna kuthawa m'nyumba zawo kumadzagona kubawa kwa a Chimwa Mowa.

Munthu wotchuka pankhani yogula ndi kumwa mowa ndi mkulu yemwe ankacheza ndi Zione tsiku loyamba lija. Dzina la mkuluyu ndi Jomeni Chikhwaya. Uyu ndiye mwamuna wodya bwino. Alibe kuti pano npakati pamwezi. Monga mwa dzina lake ndi chikhwayadi. Kupikisana naye nkungodzitayira nthawi pachabe. Iyeyu adali wamkulu m'kapani ina yake m'tauni momwemu. Vuto lake linali la akazi. Akuti adasiyapo akazi anayi. Ana ndiye ali mbwee m'taunimo.

Nthawi zambiri a Jomeni Chikhwaya kogona kwawo nkubawa kwa Chimwa Mowa komweko. Amachita kufika pomasiya zovala zawo kwa atsikana ogulitsa mowawo. Chimenechi ndi chaka chachinayi akukhala okha. Mkazi wawo wachisanu zaka zapitazo adali kamtsikana kakang'ono koma kadamwalira pangozi yomwe a Jomeni adachita ndi galimoto yawo. Galimotoyo idaonongekeratu. Kuchokera pamenepo akuti sadatolenso kena kogwa n'chiswe. Chinthu china chomwe chimawasangalatsa anthu akatulukira a Jomeni m'bawa ya "Osauka Satopa" ndi chakuti akamwa nkukhuta



ankawapempha a Chimwa Mowa kuti awayikire malekodi akalekale.

Pa atsikana atatu atsopanowa a Jomeni amakonda kucheza ndi Zione. Masiku ena akamwaimwa mowa wawowo Jomeni ankamutengera Zione kupita naye kunyumba kwawo, koma chizolowezi chawo chidali chogona kubawa komweko. Anthu ambiri odzamwa mowa kumeneko adadziwa kuti a Jomeni ndi Zione adali pa ubwenzi. Mkuluyo amamugwetseradi makwacha ambiri mtsikanayo.

Pang'onopang'ono Zione adapitirira kuoneka bwino koposa anzake awiriwo omwe amangoti lero ali ndi mwamuna uyu, mawa ali ndi wina. Mwina akafatsa Zione amawaseka anzakewo ndi kumawanena kuti saoneka bwino chifukwa chosakhazikika ndi mwamuna mmodzi.

Moyo wa anthu a mowa ndi wovuta kuumvetsa. Simungakhulupirire kuti palibe ndi tsiku limodzi lomwe pomwe a Jomeni ndi Zione adafunsanapo za kumudzi. A Jomeni sankadziwa kuti mayi wake a Zione amakhala kunsi kwa mulatho. Naye Zione sankadziwa komwe amachokera a Jomeni. Mwina akasangalala mkuluyo amamulongosolera zovuta zomwe adaziona kuti adzichita kusintha akazi ngati zovala.

"Kutereku ine zodzakwatiranso ayi," ankatero a Jomeni.

"Aaa ndiye mufuna kundiuza kuti simudzandikwatira. Inetu ntchito ya m'bawayi ndidalowera kuvutika. Nditapeza mwamuna woti watsimikiza kundikwatira ndikhoza kuchokamo ine," Zione naye ankatero.

"Kodi umadziwa kuti ine ndili ndi ana aakulu kuposa iwe?"

"Ndiye zili ndi kanthu zimenezo."

"Eee zili ndi kanthu."

"Ayi musatero a Jomeni. Inetu ndimakukondani ndi mtima wanga onse. Kodi mumadziwa kuti inu ndi mwamuna woyamba kukhala nane pa ubwenzi?"

"Choka apa Zione, ufuna kumpusitsa yani?"

"Ndithudi ndikulumbira pamaso pa Mulungu."

"Ayi amenewo ndi masewera, usamafike potchula Mulungu. Ukafuna kundinamiza zoti umandikonda, ungotero, koma osati zomatchula Mulungu ayi."

"Ndikunena zoona ndithu kuti chibadwire sindinakhalepo pa ubwenzi ndi mwamuna. Oyamba ndi ndi inuyo."

"Tionatu m'tsogolo muno ngati nzoona." Chikondi pakati pa Jomeni ndi Zione chidalimba ndithu. Kenaka eni bawa aja zidayamba kuwanyansa kuona Zione akumangokhala ndi a Jomeni osafuna kusangalatsa amuna ena odzamwa mowa m'bawamo. Adamuchenjeza kangapo koma Zione osasintha. Anzakenso adamuchenjeza kuti mwinatu a Chimwa Mowa adzamuchotsa ntchito koma iye sadawamvere.

Leleni ndi Aida adamudandaulira kwambiri chifukwa kudzera m'ntchito ya m'bawayi atsikanawo ankapita kumakawapatsa ndalama makolo awo kunsi kwa mulatho kuja. Tsono ngati ntchitoyo itatha ndiye kuti makolowo adzakhalanso m'mavuto monga kale lija. Nthawi ina atsikanawo adakawauza makolowo kuti achokeko kunsi kwa mulatho akafune nyumba za lendi, koma makolowo adakana ponena kuti kodi kunsi kwa mulathoko kwaipa lero? Kodi malo obadwira amaipa? Basi atsikanawo adasiyira pomwepo nkhaniyo, nkuwauza kuti akhoza kumakhalabe komweko ndipo adziwapatsa chithandizo monga ankachitiramo.

Zione ndi mtsikana wosamva zonena bwana wake ndi anzake aja. Chomwecho mathero ake ndiwo kuchotsedwa ntchito. Bwana wake adamuitana ndi kumpatsa malipiro amwezi umenewo nkumuuza kuti achokepo pa bawa



pawo, zamakani zakezo akapeze ntchito kwina adzikachitira kumeneko.

Izo sizinamudandaulitse Zione. Adatenga katundu wake ndi kuwatsazika anzakewo. Iwo adadziwiratu kuti Zione sangapite kunsi kwa mulatho kukakhala. Zoonadi iye adapita kwa a Jomeni. Pobwera kuchokera ku ntchito madzulo a Jomeni adapeza Zione ali pakhonde ndi katundu. Atalowa m'nyumba adayamba kucheza.

"Zikatere ndiye chiyani?" Adafunsa a Jomeni.

"Basi ntchito yatha. Andichotsa a Chimwa Mowa. Akuti chifukwa chiyani nthawi zonse ndimakhalira kukuchezetsani inu osamawasangalatsa amuna ena?"

"Ndi wopusa Chimwa Mowa, wangokhuta ndalama zanga. Monga iye zaka zonsezi samadziwa kuti ndiwe bwenzi langa?"

"Amadziwa."

"Nanga nchiyani lero lokhalokha adziti bwanji ungokhalira kucheza ndi ine? Mwina amakufuna ameneyo."

"Zondifunazo ndiye adayamba kalekale."

"Wakhuta ndalama ameneyo. Basi udzingokhala komkuno. Palibe chovuta. Ndiponso sindidzapitanso kubawa kwakeko. Ndi munthu wopanda ulemu Chimwa Mowa."

## Alowa M'banja

Banja pakati pa a Jomeni ndi Zione lidayambira pomwepo. Amayi oyandikirana nyumba sekani. Amvereke a Jomeni kuchita kufika pokwatira mtsikana wa m'bawa. A Jomeni ndi mkazi wawo ali phee. Angoti mukanenanena mutopa. Banja ndi anthu awiri.

Leleni ndi Aida adapita kumulatho kuja kukawauza mayi wake a Zione kuti mwana wawo adasiya ntchito ndi kuti adakwatiwa ndi mkulu wina wakenso dzina lake Jomeni Chikhwaya. Mayiwo adauza atsikanawo kuti akamuuze Zione kuti tsiku lina akapeza nthawi adzakawaone. Uthengawo utamufika Zione adapitadi kukaonana ndi amake.

"Ndamva kwa anzanu kuti mudasiya ntchito ndipo mudapeza mwayi wa banja, kodi nzoona?"

"Eee nzoona. Ntchito adandichotsa chifukwa choti akuti ndimacheza ndi mwamuna mmodzi yekha yemwe adali bwenzi langa. Tsono nditapita kunyumba kwake adandiuza kuti ndikhoza kukhala. Kutereku ndine mkanzi wa a Jomeni Chikhwaya."

"Kodi amunawo mudawauza za ine?" Adafunsa mayiwo.

"Ndidawauza kuti ndilibe tate, koma mayi wanga alipo, koma sindidziwa kuti ali kuti poti tidasiyana kalekale."

"Mudachita bwino. Muyambe mwakhazikika chifukwatu mukapupuluma adzangokusiyani, ali kani ndiwe mwana wamasikini, okhala kunsi kwa mulatho,



tiye choka undichititsa manyazi. Inetu kuno nkukalamba. Tsiku lina mudzangomva kuti ndapita. Tsopano ndati ndi kulangize chinthu chimodzi mwana wanga. Mwamuna amene wampezayu mgwiritse. Akadzakupatsa mwana nthawi yomweyo dzamuuze kuti mukamangitse ukwatiwo. Ngati ndikadzakhala ndili wamoyo nthawi imeneyo ndiye udzamuuze za ine. Pakadali pano udzingoti atate wako adamwalira ndipo kuli amako sukudziwa. Utatero sangakufunse zambiri. Koma kundithandiza chonde usasiye. Popita kumsika uzidzera pompano ndi kumandisiyirako tindalama ndi chakudya. Pita bwino mwana wanga."

Pokwiya ndi zomwe adachita a Chimwa Mowa pomuchotsa ntchito Zione, a Jomeni adasiyiratu zomwera mowa kubawa ya "Osauka Satopa." Hoo! Zodabwitsa izi. Kusiya kwa mowa a Jomeni ndi komweku. Ataleka kumwako nalo banjalo lidalimbadi. Pomwe chinkatha chaka m'banjamo adalandira mphatso ya mwana wamwamuna. Adampatsa dzina la Dalitso. Kubadwa kwa mwana ameneyu ndiye kudakhazikitsa banjalo pamaziko enieni. Zione adamutengera mwanayo ku mulatho kuti ambuyake ndi anthu onse kumeneko akamuone. Kudali chisangalalo amasikini kuponyerana mwanayo. Ngakhale akhungu kumachita kulimbirana kakhandako.

Zinthu zodabwitsa zikati zioneke padziko, anthu amangogwira pakamwa, kulephera kumvetsa. Anthu adangoona a Jomeni ayambapo kumapita ku Tchalitchi. Ngakhale akuluakulu a Mpingo osamvetsa kuti a Jomeni nkukhala mkhristu. Za uchidakwa zija ndiponso mbiri ya mkazi wawo yoti adagwirapo ntchito yogulitsa mowa m'bawa kuyiwalikiratu. Nkhani yosangalatsa iyi. Ndani ankadziwa kuti chidakwa ngati a Jomeni nkutembenuka mtima? Nanga ndani ankadziwa kuti mtsikana wogwira ntchito ya m'bawa nkukalowa m'Tchalitchi? Akhristu ambiri adasangalala. Nchifukwa chake pamene a Jomeni

adakafunsa abusa ngati nkotheka kukamangitsa ukwati wawo kutchalitchi adauzidwa kuti akhoza kutero. Pankhani yomangitsa ukwatiyi malingaliro a Jomeni ndi mkazi wawo Zione adali oti adzangopita kumwambo wa kutchalitchi ndipo pambuyo pake adzakhale ndi kaphwando kakang'ono kunyumba madzulo.

Kungoyitana anzawo ochepa ndi akuluakulu a mpingo basi.

Anzawo ogwirizana nawo kwambiri atamva chikonzero chimenecho adawatsutsa. Iwo adati ukwati suchepa. Ukwati wa a Jomeni ndi Zione ndi wofunikira chiphwando chachikulu kuholo osati m'nyumba. Anthu adadziperekadi kuchita msonkhamsonkha. Ndalama adapeza zambiri. Zidzakwanira bwinobwino kugulira ng'ombe, mpunga, zakumwa ndi zakudya zamitundu yosiyanasiyana. Zonse zokonzekera zitatha padali kufunika nkhoswe. A Jomeni adapempha Zione kuti apeze munthu wamwamuna adzamuyimirire. M'tauni izi sizivuta ngati kumudzi. Ena amakhoza kukatenga munthu wamba n'kukamulembetsa kuti ndi malume wawo. A Jomeni adamufunsanso mkazi waoyo ngati pangapezeke njira yoti mayi wake adzakhalepo pa ukwatiwo. Zione adawanamiza amunakewo kuti pali mkulu wina m'taunimo yemwe adakulira limodzi ndi mayi wake. Akhoza kukamupempha kudzayimirira monga nkhoswe, komanso mkulu yemweyo ndiye mwina angadziwe kuli mayi wake.

Lonselo lidali bodza. Zione adangopita kunsi kwa mulatho kukawauza amake nkhani yonseyo. Iwo adapempha mkulu wina wopuwala dzanja dzina lake akuti Ndatsala kuti akagwirizire ukwatiwo. Adabwerera kunyumba ndi chimwemwe m'tsaya.

Adamuuza mwamunake kuti, "Munthu wodzandiyimirira ndamupeza, ndiponso wati awafunafuna mayi kufikira atawapeza. Akuti ankadziwa



komwe ankakhala chaka chatha, koma adasamukira kwina."

Tsiku lina Zione adakamutenga mkulu uja atamudyetseradyetsera zonse kupita naye kutchalitchi pamodzi ndi a Jomeni. Kumeneko adagwirizana za tsiku lomangitsira ukwatiwo. Pomufunsa mkuluyo za mayi wake a Zione naye adalikuntha bodza.

"Amenewo ndakudziwa komwe akukhala. Ndi kutali kwambiri. Sikupita galimoto, koma musadandaule chifukwa ndiyesetsa kuti patsiku lalikululi adzakhale nafe. Apo pokha ndiye sindilephera, ndiyesetsa," adawatsimikizira mkuluyo.

Zione adali phee akudziwa bwino kuti mayi wake ndi anthu onse akunsi kwa mulatho ankakonzekera zodzakhala nawo pa ukwatiwu. Nthawi zina izi zinkamuopsa, komanso amati akakumbukira malo amene adabadwira ankaona kuti ndi bwino onse akumeneko adzakhalepo pa chikondwerero chimenechi. Zonsezi a Jomeni ndi abale awo sankazidziwa.

Akapeza mwayi wopita kunsi kwa mulatho Zione amazemba kukaonana ndi mayi wake, kukawauza momwe zinthu zimayendera. Patsikulotu kudzakhala kudya, kumwa ndi kuvina. Monga m'maukwati a anthu ena onse m'tauni kudzakhala mphatso za mtengo wapatali.

## Chikumbumtima

Mwina anthu nkumaganiza kuti amasikini akunsi kwa mulatho samadziwa zomwe zimachitika m'zikwati. Uko nkulakwa chabe. Ana a amasikiniwa amapita kumakasuzumira m'mazenera a m'maholo momwe amachitira maphwando a ukwati. Ena ambiri amakhoza kulowa m'kati momwemo.

Anawa ndiwo adawauza abiti Joni ndi a Ndatsala zonse zochitika ku ukwati, kuyambira kutchalitchi mpaka kuholo kochitikira phwando. Zonsezo ana a amasikini amazidziwa.

Chikonzero nchakuti Abiti Joni ndi a Ndatsala adzapita kukagona kunyumba kwa anzawo a Jomeni Chikhwaya usiku woti ukwatiwo ndi mawa. Kwa nthawi yoyamba a Ndatsala adzavala suti, nsapato ndi masokosi bwinobwino. Nawo Abiti Joni adzavala diresi lapamwamba. Zonse zogulidwa ndi a Jomeni. Koma kuli kanthu chaka chino.

Zikalata zoyitanira anthu kuti adzabwere ku chikwati cha Jomeni ndi Zione zidalembedwa motere:

.......Mukuyitanidwa ku ukwati wa Jomeni Chikhwaya, mwana wamwamuna woyamba kubadwa m'banja la malemu bambo ndi mayi Chikhwaya ndi Zione Joni, mwana wamkazi wa mayi Abiti Joni. Ukwatiwu adzaumangitsira ku tchalitchi cha .......Loweruka pa ...... Nthawi ya wani koloko masana. Pambuyo pake kudzakhala phwando kuholo ya ......Nonse mukuyitanidwa...



Uthenga umenewu udalengezedwa pa wayilesi kangapo kotero kuti anthu ambiri adamva za ukwatiwu. Oseka ankaseka. A Jomeni kuchita kufika kukwatira mtsikana wogulitsa mowa m'bawa. Naye Zione, ngakhale kusowa kwa amunako ndiye mpaka kukwatiwa ndi a Jomeni Chikhwaya mwamuna wosakhazikika ndi mkazi mmodzi. Zokamba za anthu osamazidandaula. Akalankhulalankhula nkusekaseka amadzatonthola. Chikonzero cha ukwati wa Jomeni ndi Zione chidapitirira.

Kunsi kwa mulatho nako kudali kalikiliki. Patsikulo amasikini onse adzatenga zidebe zawo ndipo adzayimba nyimbo zawo. Iwowa sadzapita nawo kutchalitchi, koma ulendo wawo udzakhala wa kuholo komwe kudzachitikire phwando. Amasikiniwa sadzayiwala zida zawo kuchitira kuti ngati wina atawaletsa kulowa m'holomo kudzakhala maferano...wafawafa.

Madzulo aliwonse amasikini ankaphunzitsana nyimbo za ukwati. Phokoso liri m'kati chomwecho Abiti Joni adalowa m'kanyumba kawo kamakatoni nkuyamba kulira. Maganizo adawadzera Abiti Joni pokumbukira kuti mwamuna yemwe adawapatsa mwana zaka zapitazo kwawo sankamudziwa. Zikadakhalatu bwino nawo atate a Zione akadadzakhalapo pa mwambo wa ukwati umenewu.

Abiti Joni adakumbukira momwe adakumanirana ndi mwamuna wina zaka zam'mbuyomo. Tsiku lina Abiti Joni kudawadera kumaganyu osinja kumalaini. Atamaliza ntchito yosinjayo adayambapo ulendo wobwerera kunsi kwa mulatho. Nthawi zambiri kosinjako ankabwerakonso ndi gaga, koma pa tsikuli adangolandira ndalama monga malipiro. Eni mphale adali atangogula nkhuku zoweta ndipo gagayo adali chakudya cha nkhukuzo. Apa panalibe chodandaulitsa kwenikweni chifukwa ngakhale zidali chomwecho Abiti Joni adapezako timakwacha titatu

malinga nkuti adasinja mitondo yambiri kusiyana ndi masiku ena.

Kuchokera kumalaini kupita kunsi kwa mulatho ndi kaulendo ndithu. Chomwecho Abiti Joni adayenda mwandawala. Adaonetsetsa kuti adziyenda m'mbali mwamsewu chifukwa cha kuwala kwa magetsi. Akuyenda chomwecho adangoona galimoto yawaimira.

Mutu atatulutsira pazenera mwini galimoto adafuula, "Mukupita kuti mayi?"

"Ku tauniku kufupi ndi kumsika," adayankha Abiti Joni.

"Kwerani msanga ndaima pachabe."

Abiti Joni adakwera galimotoyo namuuza mwamunayo kuti akhoza kuwasiya pena paliponse akafika kufupi ndi msika waukulu wam'taunimo. Anthu awiriwa sadafunsane maina. Chinthu chonga chimenechi Abiti Joni sadachionepo.

Zaka zonse zomwe adakhalira m'taunimu palibe ndi tsiku limodzi lomwe munthu adawaimira ndi kuwatenga m'galimoto. Awa ndi malodza. Abiti Joni adachita mantha.

"Kodi muli ndi malonda kumsikaku?" Adafunsa mwamunayo.

"Eee!" adayankha Abiti Joni chifukwa cha manyazi kuopa kumuuza mwamunayo zoti amakhala kunsi kwa mulatho.

"Nanga uku mukuchokera kuti usiku ngati uno?"

"Ndinapita kuganyu yosinja kumalaini ndiye kwandidera."

"Bwanji ndikutengereni kunyumba yogona alendo?" Adatero mwamunayo poyamba kuwanyenga Abiti Joni.

"Kunyumba yogona alendo? Kukatani?" Abiti Joni adafunsa.

"Mukufunsa ngati ndinu mwana bwanji?"



"Ayi sindikufunsa ngati mwana, koma ndifuna kudziwa kuti tikataniko kunyumba yogona alendoyo?"

"Ngati mutalola kupita nane kunyumba yogona alendo ndikupatsani ndalama zambiri," adatero mwamunayo atatayirira chiongolero cha galimoto.

Ooo! chabwino. Abiti Joni adazindikira chomwe mwamunayo ankatanthauza. Kani ndi zoona zomwe atsikana ena okulira kumulatho kuja ankanena zoti kumachita timaganyu ndi kutaya nthawi chabe. Mkazi akhoza kupeza makwacha ambirimbiri usiku umodzi.

Kodi nchifukwa chake akamadutsa mmalo ena Abiti Joni amaona atsikana ovala bwino, atangoimaima. Inde pena pake Abiti Joni adaona momwe atsikanawa adachitira poithamangira galimoto itaima kukhala ngati mpikisano.

Kwa Abiti Joni aka nkoyamba munthu wa galimoto kuwaimira pankhani yonga imeneyi. Adayamba akana Abiti Joni, koma mwamunayo atati awapatsa K10 adafooka navomera!

## Mwamuna Wachipongwe

Adapitadi kunyumba yogona alendo. Potuluka m'nyumbamo anthu adangoona mwamuna ndi mkazi akukangana. Eti mwamunayo anawapatsa Abiti Joni 50t m'malo mwa K10 yomwe adawalonjeza ija. Apatu nawo Abiti Joni adangoti kaya umbuli ndi wanga umenewo, koma lero andipatsa K10 yanga. Abiti Joni yambani kukokana ndi mwamunayo. Anthu ogwira ntchito panyumba yogona alendoyo thamangani. Chachitika nchiyani nanga? Mwamuna ndi mkazi si aja adabwera limodzi mwachikondi?

"Eti amenewa akundipatsa 50t pomwe adandilonjeza K10. Sindiwaleka. Andipatse ndalama zanga basi."

"Aaa iwe tandisiya unding'ambira jekete."

"Ndikuti mundipatse ndalama zanga."

"Ndilibe ndalama ine."

"Nanga mumandinamiziranji? Ndiye nditenga jekete."

Anthu oyang'anira pa nyumba yogona alendoyi adawakhalira kumbuyo Abiti Joni ndi kumuuza mwamunayo kuti awasiyiredi jeketelo. Poopa kuululika mwamunayo adavula jeketelo. Adayang'anayang'ana ngati muli china chilichonse. Adatulutsamo makiyi a galimoto ndi a nyumba yake. Adapereka jeketelo kwa mkaziyo. Mwamunayo adakakwera galimoto mokwiya nkumapita kuwasiya Abiti Joni atakumbatira jeketelo m'khwapa.



Galimotoyo itapita nawo Abiti Joni adawatsazika anthu ogwira ntchito panyumbayo, kuwasiya akumangoseka. Atafika kunsi kwa mulatho Abiti Joni adayang'anayang'ana m'matumba mwa jeketelo. Mudalibe ndalama. Atagwira pathumba la pamtima adazindikira kuti mudali ka enivelopu kakang'ono. Mwina muli ndalama. Adakatulutsa nkusuzumiramo, koma ayi mudalibe ndalama. Mwamuna uja adanenadi zoona kuti alibe K10.

Kanthu kena kake kamaoneka ngati kakanirira m'mbali m'kati mwakaenivelopuko. Abiti Joni adalowetsa zala ziwiri nkukatulutsa. Ooo! Ndi kachithunzi kakang'ono kamwamunayo kuoneka kuti kangojambulidwa posachedwapa.

Iwo sadamuonetse munthu wina aliyense kachithunzika. Za momwe adayendera usiku umenewo ndi momwe mwamuna wina yemwe sadamfunse dzina adawachitira chipongwe sadauzenso aliyense. Anthu adangodabwa kuti Abiti Joni abwera pakati pa usiku ndipo m'mawa apezeka ndi jekete la pamwamba kwambiri. Jekete la mtengo wapatali.

Tsiku lomwelo anyamata aku mulathoko adawapusitsa powauza kuti akhoza kukawagulitsira jeketelo pamtengo wabwino. Abiti Joni pusani, apatseni anyamatawo. Sadawone ndi khobidi limodzi lomwe. Anyamatawo adakagulitsa jeketelo nkudya ndalamazo.

Umutu ndi momwe Abiti Joni adapezekera ali wodwala, nabala mwana dzina lake Zione. Tate wake wa Zione ndi mwamuna amene adawatengera kunyumba yogona alendo nkuwanamiza kuti awapatsa K10. Iwo ankadziwa bwinobwino kuti chithunzi chomwe adachipeza m'thumba la jeketelo chidali cha mwamuna wa chipongwe uja, koma mwanayo adamubisira chithunzi chimenecho mpaka adakula nkuchoka kunsi kwa mulathoko kukayamba ntchito ya kubawa ija, kenaka

nkumadzatengana ndi a Jomeni Chikhwaya. Lero ndi umu akukamangitsa ukwati pa tchalitchi ali ndi mwana mmodzi.

Abiti Joni adachitenga chithunzi nkumangochiyang'anitsitsa. Tsopano chidali chili bii chosaoneka bwino chifukwa cha zaka zambiri ndiponso posungira pake sipabwino, komabe chimaoneka kuti ndi chithunzi, munthu wake utamuona ukhoza kumuyerekeza ndi wa pachithunziyo ndi kumuloza popanda vuto lirilonse.

M'zaka zonsezi iwo sadakumanepo ndi mwamuna woti nkumuyerekeza ndi chithunzichi. Ganizo la nzeru lidawafikira Abiti Joni. Chithunzi chimenechi ndi chomwe adzatenge monga mphatso ya ukwati. Akamupatsa Zione akawaone atate wake. Mphatso yaikulu, yoposa chinthu china chilichonse. Zione akakawaona atate wake ndi kumva nkhani yonse akavutika mu mtima, koma kenaka mtima wake ukakhala m'malo ndipo adzasangalala. Chithunzi chooneka kuti munthuyo pa unyamata wake adaali wokongoladi. Zione akakondweradi.

Pomati ukwatiwu ndi mawa lino Zione adabwera kudzawatenga amake pamodzi ndi a Ndatsala kuti akagonere kufupi komweko. Iwowa adakagona kunyumba ya m'nzake wa Jomeni. Chisangalalo chidali chitayambapo kale. Abiti Joni sadayiwale chithunzi chija. Adachita kukagulira envelopu nkuikamo bwino ndithu.

Tsiku la ukwatilo Abiti Joni ndi a Ndatsala adanyamulidwa pa chigalimoto chapamwamba kupita ku tchalitchi. Kwa nthawi yoyamba Abiti Joni adaona mwamuna wa Zione. Wamtali, woyera, wosunga tindevu ngati katonde. Koma kutchalitchiko adakhalira patali chomwecho sankamuona bwino nkhope yake. Zonse zidayenda bwino kutchalitchiko. Tsono ulendo wa kuholo. Kodi amenewa simaloto? N'kukhala zoona kuti ulemerero



umenewu n'kuuwona Abiti Joni? Amayi ankayimba nyimbo za mitundu zosiyanasiyana. Zambiri zofana ndi zomwe ana a amasikini aja adaphunzitsa makolo awo kunsi kwa mulatho kuja.

Kuholo kuja kudali anthu ambiri. Abiti Joni adapatsidwa mpando wapafupi ndi ankwatiwo. Pomuonetsetsa mkamwiniyo Abiti Joni adaona kuti akufana kwambiri ndi munthu wa pachithunzi, kusiyana kwake nkwakuti munthu wapachithunziyo adalibe ndevu ndi kutinso ankaoneka wachinyamata, malinga nkuti chithunzicho chidajambulidwa kalekale Zione asanabadwe.

Abiti Joni adasowa mtendere. Adatulutsa envelopu yawo ija naitsekula ndi kuchotsamo chithunzi chija. Adachionetsetsa ndi kutembenukira kwa mkwatiyo.

Gulu la amayi litayambapo kuyimba nyimbo ya "Perekani" Abiti Joni adaima ndi kupita pafupi ndi a Ndatsala. Anthu amangoti mwina akukapempha ndalama zoti akaponye m'mbale. Ayi adali ndi funso mu mtima mwawo. Adakagwada pambali pampando wa a Ndatsala ndi chithunzi chija nafunsa monong'ona, "Kodi a Ndatsala, munthu wa pachithunzi ichi simukumuona kufana ndi mkamwini wathuyu?"

"Aaa Eee, akufana," adatero a Ndatsala. "Inu mudachitola kuti?"

Abiti Joni sadayankhe, adangopita kukakhalanso pampando. Mwambowo ukupitirira nyimbo zidamveka chapatali ndithu. Ooo! ndi amasikini akunsi kwa mulatho aja akubwera tsopano. Kenaka anthu a m'holo adangoona gulu latulukira panjapo. Anthu akhungu, opuwala manja, miyendo. Ena akumachita kukwawa pang'onopang'ono. Atenga matumba awo akuda. Wina adanyamula chibini chakutha. Anyamata ndi atsikana adanyamula masamba, maluwa ndi zitsulo zonga zikwanje.
Nyimbo yawo idali iyi:

| | |
|---|---|
| *Mtsogoleri:* | Amasikini takwatira ukwati oyera.. |
| Onse: | Ayee! Ayee! |
| *Mtsogoleri:* | Opemphapempha takwatira ukwati oyera.. |
| Onse: | Ayee! Ayee! |
| *Mtsogoleri:* | Akunsi kwa mulatho takwatira ukwati oyera... |
| Onse: | Ayee! Ayee! |
| *Mtsogoleri:* | Odya za m'mabini takwatira ukwati oyera... |
| Onse: | Ayee! Ayee! |
| *Mtsogoleri:* | Akhungu takwatira ukwati oyera... |
| Onse: | Ayee! Ayee! |
| *Mtsogoleri:* | Naneeee! |
| Onse: | Nane ndidzachita wanga ukwati Oyeraaa.. |



## Mutu 12

# Chithunzi cha Mkamwini

Anyamata omwe adaikidwa pakhomo kuti adzilandira alendo adathawapo. Gulu la amasikinilo lidalowa ndi kukhala pansi kumbuyo. Anthu onse adatembenukira kumbuyoko.

Mkulu wakhungu dzina lake Kwapsa adaima ndi kufuula:

"Amasikini Ooye!"

Onse adayankha, "Ooyee!"

"Amasikini Ooye!"

"Ooyee!"

"Abale ndi alongo," adayamba kulankhula a Kwapsa. "Mwina mwadabwa ndi kubwera kwathu. Ife tabwera kuno kuchikwati cha mwana wathu Zione. Amasikini Ooye!"

"Ooyee!"

"Zione wakhala apoyo atavala chidiresi chapamwamba, chamtengo wapatali ndi mwana wathu. Adababadwira kunsi kwa mulatho kufipi ndi kumsika, adakulira kumeneko ndipo lero walowa m'banja. Amasikini Ooyee!"

"Ooyee!"

Anasumbulera adaima nkuyambitsa nyimbo anthu onse m'holomo atangogwira pakamwa kudabwa ndi zomwe zinkachitikazo.

| | |
|---|---|
| *Anasumbulera:* | Wamkulu ndani m'banja? |
| Onse: | Wamkulu m'mwamuna! |
| *Anasumbulera:* | Wamkulu ndani m'banja? |

| | |
|---|---|
| Onse: | Wamkulu m'mwamuna |
| *Anasumbulera:* | Amasikini adzatani? |
| Onse: | Amasikini adzalira, adzalira, adzalira mwana wathu suyo, suyo, suyo walowa m'banja. |
| *Anasumbulera:* | Abiti Joni adzatani? |
| Onse: | Abiti Joni adzalira, adzalira, adzalira Zione wanga suyo, suyo, suyo walowa m'banja. |

Anasumbulera adakhala pansi ndipo a Kwapsa adapitiriza kulankhula, "Abiti Joni omwe akhala kutsogolowo, amake a Zione, chiphadzuwa mukukwatitsa lerochi, timakhala nawo kunsi kwa mulatho mpaka lero lino. Koma pali chinthu chimodzi chomvetsa chisoni. Ndicho chakuti tate wake wa Zione ife sitimudziwa. Abiti Joni adapezeka wodwala, koma adakana kutiuza mwini pakatipo."

Nthawi yomweyo Abiti Joni adanyamuka pampando pomwe adakhalapo ndi kufuula, "Tate wa mwanayu mumudziwa lero. Ndili ndi chithunzi chake. Ndachitenga kuti ndimpatse Zione monga mphatso ya pa ukwati wake.

"Musadandaule abale anga, tate wa Zione mumuona pachithunzi. Ndidakumana naye mwamunayu kamodzi. Adandipatsa pakati ine osamudziwa, adandichita chipongwe. Munthu wovutika ngati ine adangonditola panjira ndikuchokera kuganyu yosinja kumalaini, nkundichita chipongwe, nkundithawa. Mwamwayi wanga ndidamulanda jekete ndipo m'jeketemo ndidapezamo chithunzi. Muchiona lero. Papita zaka zambiri, taonani Zione lero walowa m'banja. Nyimbo kumeneko abale anga a kunsi kwa mulatho."

*Wamkulu ndani m'banja?*
*Wamkulu mmwamuna*
*Amasikini adzalira, adzalira, adzalira*
*Mwana wathu suyo, suyo, suyo*



*Walowa m'banja.*

Pomva zolankhula za Abiti Joni a Jomeni Chikhwaya adanjenjemera kwambiri. Abiti Joni adachitulutsa chithunzicho nkuchiyang'anitsitsa. Tate wake wa Zione ndi ameneyu. Kale limenelo akadali mnyamata. Mwamuna wokongola. Adakakhala mkazi tikadati nchiphadzuwa. Adachigwira chithunzicho ndi manja awiri atachiyika pamtima ndipo adalira. Muholomo mudangoti zii. Anthu kumangoonerera zochitikazo.

"Atate wako ndi awa," adatero Abiti Joni uku akumupatsa Zione chithunzicho misozi ili mbwee.

Mmalo momuonetsa mwamuna wakeyo chithunzicho Zione adayitana amasikiniwo kuti abwere kutsogoloko, "Idzani muone abale anga, thamangani muwaone atate wanga. Mwina nkukhala ali mom'muno. Ngati alipo chonde aime asachite manyazi. Aime tidziwane."

Amasikiniwo akuti adzibwera kutsogoloko Abiti Joni adaima ndi kuwaletsa, "Yambani mwakhala komweko. Zione mpatse mwamuna wakoyo poyamba awaone atate wako." Zione adapereka chithunzicho kwa amuna ake a Jomeni Chikhwaya.

Mwamunayo adachiyang'anitsitsa chithunzicho ndi kuyamba kulira. Anthu adangoona a Jomeni adzuka pomwe adakhalapo ngati munthu wozungulira mutu. A Jomeni adayamba kufuula, "Mayo ine ndakwatira mwana wanga. Nditani ine? Ndakwatira mwana wanga."

"Watani?" Adafunsitsa Abiti Joni.

"Mayo ine ndakwatira mwana wanga. Ichi ndi chithunzi changa ndikadali mnyamata," adatero a Jomeni.

Abiti Joni adawadumphira a Jomeni uku akulalata, "Mfiti iwe, nyama ya kuthengo. Ndipatse chithunzicho kuno." A Jomeni adatenga chithunzicho nachiponyera m'kamwa ndi kuchitafuna dzolimba n'kuchimeza. Abiti Joni ali nawo a Jomeni kuwagwetsa pansi. Wafuula

Jomeni. Walira mwana wa mwamuna. Abiti Joni amuluma mphuno Jomeni kungotsalira pang'onong'ono kuikhadzula. Anthu pomati tiyeni tileretse a Jomeni magazi nkhope yonse ndipo akomokeratu.


Chipwirikiti ponsepo. Amasikini yambani kumenya aliyense. Kuswa chilichonse muholomo. Anthu onse balala. Ana awo sonkhanitsani zakudya, zakumwa, nkuzithira m'matumba awo basi onse paulendo wobwerera kunsi kwa mulatho akuimba:

*Mwapalamula chitedze lero chidzakuyabwa...*
*Amasikini adzalira, adzalira, adzalira...*
*Perekani, perekani, perekani, mukapanda kupereka...*

Abiti Joni ndi mwana wawo Zione adali nawo pa gululo kubwerera kunsi kwa mulatho. Anyamata anayi athanzi adawatenga a Jomeni Chikhwaya ali chikomokere. Asanafike kunsi kwa mulatho kwawoko apolisi atulukira. Amasikini onse balala. Abiti Joni nkusadziwa kuthamanga kwawoko kalekale ali m'manja. A Jomeni Chikhwaya adakatsitsimukira ku chipatala mphuno ili magazi okhaokha.

Fikani nthawi ya mulandu mavuto Abiti Joni. Nkhani yawo ndi yomveka ndithu, koma chithunzicho chili kuti? Palibe adachitafuna a Jomeni nkuchimeza. Komadi nzoona kuti a Jomeni adakwatira mwana wawo? Eee nzoona, ngakhale a Jomeni eni ake adavomera. Poti zili choncho mulandu wa Abiti Joni ndi woluma mphuno a Jomeni. Ichitu ndiye chifukwa chake Abiti Joni ali kundende. Adawagamula kukagwira ntchito ya kalavula gaga.

Anthu omwe adapita ku ukwati umenewo sadzayiwala zomwe adaziona patsikulo.



*Willie T. Zingani*

Zochitika padziko lapansi nzambiri. Zina ukazimva umatsutsa kuti ayi sizingachitike. Kodi nkutheka munthu kukwatira mwana wake m'chimbulimbuli? Ena nkumati izo ndi nkhambakamwa, munthu sangakwatire mwana wake.

Nanga omwe akudziwa bwino makhalidwe a anthu anganenepo chiyani? Zikhozadi kuchitika kuti munthu wapezeka atakwatira mwana wake mosazindikira. Zimenezi nzomwe adaziona a Jomeni Chikhwaya m'bukhu la "Idzani Muone".

A Zingani amachokera m'mudzi mwa a Maya m'boma la Ntchi Iwowa adabadwa pa March 1954. Maph nziro apulayimale asekondale adaw chitira ku Machin Mangochi ndi Ntchi Kenaka adapita Zambia ndipo pambu pake ku Engla komwe adakaphunz kalembedwe kankha za m'nyuzipepala kakonzedwe ka m buku.

Kuchokera m'chaka c 1973 a Zingani agw ntchito monga mkon wa mabuku m'bung la Christian Literatu Association in Mala (CLAIM), mkonzi nyuzipepala ya Mala News, mkulu dipatimenti yofalit nkhani za chituku m'bungwe la Wor Vision Internation kuno ku Malav Tsopano iwowa n wamkulu woyang'ani ntchito za CLAIM.

CHICHEWA CREATIVE SERIES